# KULANKHULA NDI MULUNGU

An AEAM Theological Commission Text

Loyamba

Grace ndi Fred Holland

# KULANKHULA NDI MULUNGU

An AEAM Theological Commission Text

Loyamba

Grace ndi Fred Holland

# KULANKHULA NDI MULUNGU

Grace ndi Fred Holland

Buku la Chichewa
Lomasulidwa ndi Baptist T.E.E.
P.O. Box 467
Lilongwe, MALAWI

Losindikizidwa ndi
Baptist Publications
P.O. Box 444
Lilongwe, MALAWI

Mulembi - Mayi Grace Pamodzi ndi Bambo Fred Holland - 1972

Palibe munthu aliyense amene amaloledwa kutenga gawo laliku-lu kapena lochepa popanda chilolezo chochokera ku Evangel Publishing House ndi AEAM Theological Commission.

Chilolezo chomasulira buku ili mzinenero zosiyanasiyana mu Africa chidzavomerezedwa pamene pempholo lalembedwa m'kalata yofunsa mabungwe onse a Evangel Publishing House. Kukhoza kukhala kuswa lamulo la olemba bukuli ngati litamasulidwa popanda chilolezo chimenechi mokwanira.

Pamene mukupempha kuti mumasulire bukuli, chonde tchulani dzina lanu, mpingo wanu kapena mishoni yanu, dzina la ota-nthauzira ndi keyala yanu yeniyeni.

Mawu a Mulungu amene analembedwa m'bukuli anachokera mu New English Bible.

Kusindikizidwa koyamba: February, 1972
Kusindikizidwa kwachi-
ŵiri ndi kukonzanso: March, 1973
Kusindikizidwa kachitatu: June, 1974

Losindikizidwa ku Kenya
ndi Evangel Press, P.O. Box 1015, Kisumu
kwa
Evangel Publishing House, P.O. Box 969, Kisumu
imene inakhazikitsidwa ku Nyang'ori.

## MAWU OYAMBA

Buku ili ndi zochitika zatsopano. Buku limeneli ndi loyamba kupereka maphunziro a Buku Lopatulika okonzedwera mipingo ya mu Afrika mwa njira yakuti ingathe kugwiritsidwa ntchito tsiku lililonse ku maphunziro apanyumba ndi misonkhano ya Sabata lililonse.

Njira yophunzitsira maphunziro a m'buku limeneli imatchedwa ndi dzina lakuti MALANGIZO WOKONZEDWERATU (Programmed Instruction). Njira yophunzitsira kupyolera kuzokambirana za Sabata iliyonse imatchedwanso dzina lakuti Maphunziro a Mawu a Mulungu Otumizidwa kwa Gulu la Ophunzira (Theological Training by Extension). Ntchito ya phunziro la mtundu uwu idalimbikitsidwa ndi bungwe limene lidziŵika ndi dzina lakuti M'gwirizano Wofalitsa Uthenga Wabwino wa mu Afrika ndi Madagasker (AEAM). Poyamba bungwe limeneli linali kudziŵika ndi dzina lakuti, (Association of Evangelical Bible Institutes and Colleges in Afrika and Madagascar, AEBICAM).

AEAM ndi gulu limene lili la Akhristu amene amafuna kugwirira ntchito pamodzi kupyolera m'kuuzana nkhani, ubale, ndi kulimbikitsana pa ntchito yophunzitsa abusa ndi akulu ampingo mu Afrika muno.

Mu 1970 AEBICAM inagwirizana ndi Bungwe Lothandiza maphunziro a Mishoni Kutsidya kwa Nyanja (American) pophunzira mmene angathere kugwiritsa ntchito Maphunziro a Mawu a Mulungu Otumizidwa kwa Gulu la Ophunzira ndi mmene angathere kulemba Malangizo Wokonzedweratu. Kuyambira pamenepo, alembi akhala akukomana kuphunzira malembedwe a maphunziro ena atsopano m'mizinda yosiyanasiyana mu Afrika muno.

Zasonyezedwa kuti maphunziro okonzedwa a Buku Lopatulika angakhale njira yofunika kwambiri yophunzitsira abusa ndi atsogoleri a m'mipingo ya mu Afrika muno. Buku la maphunziroli limapatsa maphunziro akunyumba ndipo misonkhano yokambirana ya Sabata ndi Sabata imapatsa mpata wa kukhala ndi malo amodzi ofanizira maphunziroŵa ku moyo ndi mavuto omwe amapezeka mumpingo kaŵirikaŵiri.

Maphunziroŵa adayesedwa ndipo adapezeka kuti ndi wothandiza mu Afrika. Mutu wa nkhani iyi ya mapemphero, inagwiritsidwa ntchito ndi ophunzira wopititsa mtsogolo okwanira makumi

asanu (50) m'malo wosiyanasiyana asanu pa nthaŵi yopitirira masabata khumi. Ndipo adaonetsetsa zochita za ophunzira, ndiponso maphunziroŵa adakonzedwanso kuti asindikizidwe. Uku ndi kusindikiza kwachiŵiri kwa maphunziro ameneŵa. Maphunziroŵa akonzedwanso bwinobwino kuchokera m'buku loyamba.

Nkofunika koposa kuti maphunziroŵa ayesedwenso ndi kupititsa mtsogolo njira zolembera maphunziro okonzedweratu woyenera mu Afrika muno.

Tsopano kukupangidwa maphunziro olemba mabukuŵa, ndipo pakali pano mabuku ena oposera pa chiwerengero cha makumi aŵiri ali mkati kulembedwa. Kukuyembekezeka kuti posachedwapa tidzakhala ndi dongosolo la maphunziro onse ofunika kuphunzira Buku Lopatulika.

Fred Holland
Secretary for Theological Education
AEAM Theological Commission
P.O. Box 131
Choma, Zambia

MMENE MUNGAGWIRITSIRE NTCHITO BUKU ILI

Buku ili limakuthandizani kuphunzira kupemphera moyenera. Sikuti ndi ulaliki wa kupemphera ayi, kapena nthano za momwe Mulungu amayankhira pemphero ayinso. Ili ndi buku la maphunziro anu, kotero kuti mudziŵe zimene Buku Lopatulika limaphunzitsira, ndi kutinso muzichita zimene Buku Lopatulikali limanena. Mukatsiriza buku ili muyenera kumapemphera mwa njira yatsopano.

Buku limeneli ndi mphunzitsi wanu. Lidzalankhula nanu pa maphunziro anu a tsiku ndi tsiku. Mumvetsetse bwinobwino zimene likunena. Pamene mphunzitsi akuuzani kuti mutenge Buku Lopatulika lanu ndi kuwerenga ndime, kodi mumachita chiyani? Kodi mumangomuyang'ana, kapena mumanena kuti ayi ndidzawerengabe patsogolo pano? Ayi, mumatenga Buku lanu Lopatulika ndikumawerenga. Chimenechi ndi chimene muyenera kumachita ndi buku ili.

Penyetsetsani zimene amachita mphunzitsi m'sukulu. Iye amaŵauza phunziro ophunzirawo. Iye amalimasulira bwinobwino phunziroli. Pambuyo pake amafunsa mafunso. Ophunzirawo akayankha bwino, iye amaŵauza kuti mwayankha bwino. Koma akapanda kuyankha bwino, mphunzitsi uja amaŵafotokozeranso phunzirolo kachiŵiri.

Bukuli limaphunzitsanso chimodzimodzi. Choyamba mumapatsidwa mbali imodzi ya phunziro. Kenaka mumakhala ndi funso lakuti mufunse kapena china chake chakuti muchite. Mudzatha kuyankha bwino ngati mwaŵerenga bwinobwino. Kuyankha funso kumapanga zinthu ziŵiri. Choyamba kumakusonyezani ngati mwalimvetsetsa bwino. Chachiŵiri, kumakuthandizani kukumbukira zomwe mwawerenga.

Choncho bukuli lili monga mphunzitsi, limakuuzani ngati yankho lanu lili lokhoza kapena lolakwa. Kodi limachita zimenezi bwanji? Pomaliza pa phunziro lililonse mudzapezapo mayankho a mafunso a phunziro limenero. Mukatha kulemba, muzipenya kumayankho ndikuona mmene mwalembera.

Koma vuto ndi lakuti, nthaŵi zina mumanyengedwa kupenyera kumayankho pamene musanalembe. MUYENERA KUKHALA OSAMALIRA KWAMBIRI KUTI MUSAMACHITE ZIMENEZI. Ngati muchita zimenezi ndiye kuti mudzaononga maphunziro anu. Simudzapweteka mphunzitsi wanu, koma mudzadzipweteka nokha. Mudzakhala ngati wophunzira amene amaba mayankho kuchokera ku mapepala anzake m'malo moti adzilembere yekha mayankho ake. Nthaŵi zambiri wophunzira wa mtundu ngati ameneyu saphunzira bwino. Muyenera kukhala okhulupirika. Ife tayesa kukuthandizani mwakuphiphiritsa kapena kuti kusakaniza mayankhoŵa kuti musaŵaone nsanga isanafike nthaŵi yake.

Ndipo kumbukirani kuti mudzalemba mayeso pakutha pa maphunzirowa. Ndiye ngati mukubera mayankho, mudzapeza mavuto pofuna kuti mupambane mayeso anu. Nthaŵi zina mungathe kudzapeza mavuto poganiza za yankho lake. Koma musayang'ane payankho la mphunzitsi, koma werenganinso mbali ya phunzirolo kachiŵiri. Werengani pang'onopang'ono ndi mosamalitsa mpaka mutakwanitsa kuyankha funsolo.

Maphunziro amaperekedwa pa sabata lililonse ndi masiku onse. Muyenera kuwerenga phunziro la tsiku limodzi pa nthaŵi imodzi. Osawerenga mbali ya phunziro ndi kusiyira padera osamaliza. Mudzaphunzira kwambiri ngati mutatsiriza phunziro lonse pa tsiku la thunthu. Osachita maphunziro a sabata la thunthu pa nthaŵi yochepa. Mudzangofulumira kuwerenga nsanga ndi pamene simungakumbukire bwino zimene mwaziwerengazo. Tayesani kuchita phunziro la tsiku limodzi pa tsiku lililonse, monga mmene mumamvera pa phunziro la tsiku ndi tsiku kuchokera kwa mphunzitsi wanu.

Bukuli lakonzedwa kuti likuthandizeni. Ndipo lizigwiritsidwa ntchito pa msonkhano wa sabata lililonse. Mudzakhala ndi mtsogoleri wanu amene adzakuthandizaninso pamavuto anu. Iyeyo adzakuthandizaninso kuti muzikambirana ndi ophunzira ena za zimene mwaziphunzira m'bukuli. Ngati musanaphunzire phunziroli musabwere ku msonkhano chifukwa simudzamvetsetsa zomwe zidzakambidwe.

Ngati palibe mtsogoleri amene angabwere kudzalankhula nanu za maphunzirowa, ndiye kuti muitane ena mwa abwenzi anu omwe akuphunzira bukuli. Sankhani wina pakati panu kuti akutsogolereni zokambiranazi.

Tikuganiza kuti kuphunzira kwa mtundu uwu mudzakukonda. Mukamaphunzirabe mudzayesetsa kupeza mayankho oyenera Ndipo mudzakondwera ngati mutaŵapeza. Mukafika kumafunso a kothera kwa bukuli mudzaona mmene mwaphunzirira. Mulungu akudalitseni pamene muli kuphunzira kupemphera bwino.

ZA MKATIMU

MMENE MUNGALIGWIRITSIRE NTCHITO BUKU ILI

| | | |
|---|---|---|
| Sabata Loyamba: | Kodi Pemphero ndi Chiyani? | 6 |
| Sabata Lachiŵiri: | Kodi Nchifukwa chiyani Tiyenera Kupemphera? | 20 |
| Sabata Lachitatu: | Kodi Tiyenera Kupemphera Nthaŵi Iti? | 37 |
| Sabata Lachinayi: | Kodi Tiyenera Kupempherera Chiyani? | 56 |
| Sabata Lachisanu: | Kodi Tizipemphera Bwanji? | 78 |
| Sabata Lachisanu ndi Chimodzi: | Kodi Chimalepheretsa Mapemphero Kuyankhidwa ndi Chiyani? | 102 |
| Sabata Lachisanu ndi Chiŵiri: | Kukula M'Chikhulupiriro | 120 |
| Sabata Lachisanu ndi Chitatu: | Kupemphera ndi Anthu Ena | 144 |
| Sabata Lachisanu ndi Chinayi: | Mayankho a Mapemphero | 163 |
| Sabata la Khumi: | Pemphero La Ambuye ndi Kubwereza | 184 |

SATABA LOYAMBA: KODI PEMPHERO NDI CHIYANI?
TSIKU LOYAMBA:

"Pemphero" ndi liwu limene Akhristu amaligwiritsa ntchito polankhula pafupifupi tsiku lililonse. Ndi chinthu china chake chomwe chakhala ngati mbali ya umoyo wa Chikhristu. Tikamauka m'mawa timapemphera. Timapemphera tikamadya chakudya. Timapemphera ndi banja lonse madzulo. Timapemphera poyamba msonkhano wathu ku tchalitchi ndipo potsiriza timatsekanso ndi mapemphero.

Koma mukafunsa anthu ena kuti pemphero ndi chiyani, iwo amapeza kuti nkovuta kukuuzani. Iwo amayankha mayankho ambiri osiyanasiyana.

1. Kodi mukuganiza kuti anthu ambiri amalimvetsetsa bwino tanthauzo lake la pemphero?

__________________________

==========================================================

Buku Lopatulika limatiuza nthaŵi zambiri kuti tizipemphera. M'maphunziro aŵa tifuna kuti tione ndime zina m'buku Lopatulika zimene zimatiuza kuti tizipemphera. Tikufuna kuti timvetsetse bwinobwino zimene Mulungu amanena kuti pemphero ndi chiyani.

2. Kodi inu mumaganiza kuti pemphero ndi chiyani?

________________________________________________________

==========================================================

Pemphero ndi lalikulu kwambiri ndiponso lokhwima pofuna kulimasulira pa mawu ochepa. Anthu ena amadziŵako pang'ono magawo ena a kamasulidwe kapemphero. Komabe sadziŵa magawo onse akamasulidwe kake. Mwina mwake inunso muli ngati anthu oterewo. Kapena mumadziŵa zinthu zina zake za pempheroli. Komabe muyenera kuphunzira zambiri.

3. Kodi mukufuna kuphunzira zambiri za pemphero?

______________________

==========================================================

Tili ndi maphunziro amenewa chifukwa tikufuna kuti tiphunzire zambiri za pemphero. Mulungu amati adzachita zinthu zodabwitsa pofuna kuyankha pemphero. Koma sitimuona Iye akuchita monga momwe ife tifunira. Kapena vuto lake ndi lakuti sitimtha kupemphera bwinobwino. Tiyeni tiyese kuphunzira bwino.

4. Potsiriza phunziro ili gwetsani nkhope yanu ndikupempha Mulungu mosamala kwambiri kuti akuthandizeni kuphunzira maphunzirowa kuti muthe kuphunzira bwino mmene mungapempherere.

************************************************************

MAYANKHO

2. Bwerani ndi buku lanu ku kalasi ndipo tidzakambirana za yankho lanu.
1. Ndinakufunsani chimene mukuganiza, choncho yankho lanu lili lokhoza. Koma kwa ine, sindiganiza kuti anthu amamvetsetsa bwino.
3. Ndili wokondwa ngati mwanena kuti Inde.

SABATA LOYAMBA: KODI PEMPHERO NDI CHIYANI?
TSIKU LACHIŴIRI:

Kodi dzulo mudapemphera kwa Mulungu kumufunsa kuti akuthandizeni kuphunzira maphunziro akapempheredweŵa? Ngati mudatero, choncho yembekezani kuphunzira, chifukwa Mulungu amati adzatichitira zinthu pamene tizipempherera zinthuzo.

Lero tiyeni tione zina mwa zinthu zimene anthu amaganiza kuti ndilo pemphero. Liwu ili lakuti "pemphero" kwa anthu ena limangotanthauza kuti "Kupempha." Amati kupemphera ndiko kupempha Mulungu kuti amupatse kanthu kena.

1. Kodi kupempha Mulungu kuti atipatse kanthu kena ndi mbali ya pemphero?

   ______________________________

=============================================================

Inde, kupempha Mulungu kuti atipatse kanthu kena ndi mbali imodzi ya pemphero. Anthu ena amaganiza kuti pemphero ndi kungopempha Mulungu chinthu chimene akufuna, akatero atsiriza. Koma kupemphera kuposera apa chifukwa kupemphera sikungopempha chinthu chimene tikufuna kokha ayi.

2. Kodi ndapemphera pemphero labwino pamaso pa Mulungu ngati ndangopempha kokha kuti andithandize kuphunzira?

   ______________________________

=============================================================

Tiyeni tione ngati tingaphunzire zina zake kwa anthu amake dzana. Pamene kanthu kena kofunika kaoneka m'miyoyo mwawo, iwo anali ndi njira yawo imene anali kupempherera kwa mizimu ya makolo awo. Ngati mwana watsopano wabadwa, anthu ena ankavumata madzi kapena moŵa nalabvulira kunja pafupi ndi khomo la nyumba. Iwo ankapempha mizimu kuti imusamale bwino mwanayo. Ngati wina wadwala, ankapereka chakudya kapena moŵa kwa mizimu ndikupempha kuti imuchiritse bwino. Anthu ena ankapereka nkhuku kapena mbuzi kwa mizimuyo ngati akufuna kukapemphera.

3. Kodi ndi chifukwa chiyani anthu ameneŵa ankapereka nsembe kwa mizimuyo? Nanga ndi chifukwa chiyani anthu ameneŵa sanali kungopempha zinthu zimene anali kuzifuna?

___________________________________________

==================================================

Anthu ameneŵa ankaganiza kuti mizimu ya makolo awo ingaŵathandize. Buku Lopatulika limatiuza kuti sitiyenera kulankhula ndi mizimu ya anthu akufa. Koma ngakhale kunali choncho kuti anthu amake dzanawo samapemphera kwa m'thandizi weniweni, iwowo akhoza kutiphunzitsa kanthu kena. Iwo amatiphunzitsa kuti ngati tikufuna munthu wamkulu kuti atithandize sikwabwino kungopempha zinthu zimene tikuzifuna. Tiyeneranso kuonetsa ulemu.

Kodi mungaganizire njira zina zimene tingasonyezere ulemu kwa Mulungu mu mpemphero? ______________________________

==================================================

Ngati tifuna kupemphera bwino, tisamangopempha zinthu koma tiyenera kusonyeza ulemu kwa Mulungu pomuthokoza ndi kumulemekeza. Tiyenera kumuuza kuti timamukonda ndipo tifuna kumutumikira Iye. Choncho pamene tikunena za kupemphera zingakhale zabwino kumanena kuti kulankhula kwa Mulungu.

5. Kodi liwu limene limafotokoza bwino za pemphero koposa ndilo liti---kunena kuti pemphero ndiko kulankhula kwa Mulungu, kapena kunena kuti pemphero ndiko kupempha Mulungu?

___________________________________________

==================================================

Komatu mvetsetsani bwino tsopano. Palinso chinthu china cholakwika ponena kuti pemphero ndiko <u>kulankhula kwa Mulungu.</u> Pamene anthu amake dzana anali <u>kulankhula kwa mizimu ya makolo awo</u>, mizimuyo siinali kunenapo kanthu kali konse kwa iwo. Anthuwo anali kungofuna kuti mizimuyo iŵathandize.

Koma Mulungu amati m'Buku Lopatulika adzayankha ana ake pamene adzalankhula kwa Iye.

Yeremiya 33:3:

> Ngati utandiitana Ine, Ine ndidzakuyankha iwe ndipo ndidzakusonyeza iwo zinthu zazikulu ndizolakika zimene iwe siuzidziŵa.

6. Kodi tidziŵa bwanji kuti Mulungu adzatiyankha mmene tilankhula kwa Iye?

________________________________________

______________________________________________________

==================================================

Tidzamumva Mulungu akutiyankha ndikutiphunzitsa ngati titamamvetsetsa bwino pamene tikupemphera. Mwa ichi sitiyenera kunena kuti kupemphera ndi kungolankhula chabe kwa Mulungu. Ife timafuna njira yabwino yotifotokozera za kulankhula ndi Mulungu, ndipo amalankhulana nafe. Kodi timatcha chiyani pamene tikhala pansi ndikumalankhula ndi munthu wina ndikumpatsa nthaŵi munthuyo yakuti alankhule nafenso? Timanena kuti tikulankhula tonse pamodzi. Kodi imeneyi sinjira yabwino yofotokozera za pemphero? Tiyenera kunena kuti pemphero ndi kulankhula ndi Mulungu.

7. Kodi ndi pemphero labwino ngati ndingolankhula chabe kwa Mulungu koma osatenga nthaŵi yakuti ndimvetsere zimene Mulungu akunena?

____________________________

==================================================

8. Kodi njira yabwino kwenikweni yomasulira pemphero ndi iti? Pemphero ndi

____________________________________

==================================================

*************************************************************

MAYANKHO

5. Pemphero ndilo kulankhula kwa Mulungu.
2. Ayi, pemphero limaposa kupempha.
7. Ayi.
3. Tidzakamba izi m'kalasi.
6. Iye amatero m'Buku Lopatulika kuti adzatiyankha.
1. Inde.
8. Kulankhula ndi Mulungu.
4. Pali njira zambiri. Timasonyeza ulemu pogwada, kapena pamene tili chiimire. Timasonyeza zimenezi kwambiri pakumuthokoza ndi pakumulemekeza Iye.

SABATA LOYAMBA: KODI PEMPHERO NDI CHIYANI
TSIKU LACHITATU:

Dzulo tinaphunzira kuti kupemphera sikungopempha zinthu kwa Mulungu. Tinaphunziranso kuti pali mbali zina za pemphero. Kupempha ndi mbali imodzi yokha ya pemphero.

1. Kupatulako kupempha, kodi chinthu china ndi chiyani chimene tikanayenera kunena pa pemphero?

___

==========================================================

Inde pali zinthu zambiri zimene tingathe kunena pamene tikupemphera. Tidzakhala tikuphunzira zambiri za zimenezi m'maphunzirowa. Kunena zoona, pali zinthu zambiri zoyenera kunenedwa m'mapemphero, kotero kuti anthu ena amaganiza kuti ayenera kutalikitsa mapemphero awo pofuna kuti apemphere bwino. Iwo amaganizanso kuti ayenera kulankhula kwambiri kapena kulalikira kwa Mulungu pamene alikupemphera.

2. Ngati kupemphera kuli kulankhula ndi Mulungu, kodi tiyenera kulalikira kwa Mulungu pamene tiri kupemphera?

___

==========================================================

Anthu amene amapemphera chomwechi amaganizanso kuti ayenera kugwiritsa ntchito mawu aakuluakulu pofuna kuti mapemphero awo azimveka bwino kwa Mulungu. Iwo amayesa kugwiritsa ntchito mawu amene amaŵamva kwa anthu ena akunena popemphera Kapena kuti amayesa kugwiritsa ntchito mawu amene amangogwiritsidwa ntchito m'tchalitchi. Iwo amaganiza kuti mawuŵa amamveka bwino kwa Mulungu.

3. Kodi mukuganiza kuti Mulungu amamva mapemphero anu pamene mukugwiritsa ntchito mawu ozama?

___

==========================================================

Kodi mukamalankhula ndi mnzanu mumatani? Simungowereweta kapena kulalikira, kapenanso kuyesa kugwiritsa ntchito mawu ozama. Koma mumangomuuza zimene mukuganiza. Mumamufunsa mafunso. Mumamva zimene amanena. Umu ndimo mmene zikanayenera kukhalira pamene tikupemphera.

4. Kupemphera ndiko kulankhula ndi ________________

==========================================================

Kodi kupemphera kwa mtundu umenewu kukuoneka kusiyana ndi mmene munaganizira kuti pemphero linalili poyamba? Mukuona, pamene tikulankhula ndi Mulungu sitiyenera kuopa kuti mwina sitinena mokhoza. Sitiyenera kukhala ndi mantha akuti mwina mwake Iye sangathe kumva zimene tikunena. Timalankhula naye chifukwa chakuti Iye ndiye bwenzi lathu. Monga amanenera Mawu a Mulungu.

Yohane 15:14:
Ndinu abwenzi anga ngati muzichita zimene ndikulamulirani.

5. Kupemphera ndi ______________________________

==========================================================

Kupemphera kumaphatikiza zinthu zambiri. M'maphunziro otsatiraŵa tidzalankhula za zinthu zina zimene tizidziŵa kale ndi zinthu zina zatsopano zimene tiyenera kuziphunzira. Koma kumbukirani njira yachidule yomasulira bwino tanthauzo la pemphero.

5. Kodi pemphero ndi chiyani?

______________________________________________

==========================================================

Tsopano ine ndifuna kuti muyese chinthu china chake. Mwakhala mulikugwiritsa ntchito liwu lakuti pemphero. Kwa masabata ochepa akubweraŵa, nthaŵi iliyonse mukamaganiza za liwu lakuti pemphero ndifuna kuti muyambe mwaleka ndipo munene mawu akuti Kulankhula ndi Mulungu. Ngati mukuganiza kuti, "Ndiyenera kupemphera," dziuzeni nokha kuti, "Ndiyene-

ra kulankhula ndi Mulungu." Ngati mufuna kuuza anthu ena kuti, "Tiyeni tipemphere," lekani ndipo munene kuti, "Tiyeni tilankhule ndi Mulungu." Ichi chidzakuthandizani kuzindikira kuti kupemphera sikungopempha kapena kumangolankhula kokha ayi. Uku ndikukambirana ndi Mulungu.

*************************************************************

MAYANKHO

4. Mulungu.
2. Ayi, kulalikira kuli kosiyana ndi kulankhulana pamodzi.
6. Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu.
5. Kulankhula ndi Mulungu.
3. Ngati mwanena kuti inde, ndiganiza kuti mudzaphunzira bwino m'maphunziro ameneŵa.
1. Tiyenera kumuthokoza ndi kumulemekeza Mulungu.

SABATA LOYAMBA: KODI PEMPHERO NDI CHIYANI?
TSIKU LACHINAYI:

Taphunzira kuti anthu ambiri ali ndi maganizo olakwika pa za pemphero. Iwo amaganiza kuti ndi kupempha kapena kulalikira kwa Mulungu. Koma tsopano tikumvetsetsa bwino.

1. Kodi kupemphera ndi kutani?

______________________________________________

==================================================

Chingakhale kuti ndi kwabwino kwa ife kulankhula ndi Mulungu monga bwenzi lathu, koma sitiyenera kuiwala kuti Iye ndi wamkulu kwambiri. Iye ndiye amene anapanga dziko lapansi. Iye ndi amene anatipatsa moyo. Iye ndi Woyera. Ngati Mulungu ali wamkulu ndi woyenera, kodi anthu anayamba bwanji kulankhula naye?

Ngati titapenyetsetsa m'Buku Lopatulika timaona Mulungu kuti ndiye amene anayamba kulankhula ndi munthu. Pachiyambi kunali kwapafupi kwa Mulungu ndi munthu kulankhulana. M'munda wa Eden, Adamu analibe tchimo lililonse poyamba. Iye analibe mantha ndi Mulungu. Mulungu anali kumatsika nalankhulana ndi Adamu m'munda.

2. Kodi kuteroko kunali kupemphera pamene Mulungu ndi Adamu anali kulankhulana?

__________________

==================================================

Koma kuchokera pa nthaŵi imene Adamu adachimwa ndi kutuluka m'munda muja sitiwerenga kuti anali kulankhulanso ndi Mulungu monga m'mene anali kuchitira poyamba m'munda muja. Iye anadzilekanitsa yekha ndi Mulungu. Ichi ndi chimene Mulungu adanena kuti chidzaoneka ngati Adamu ndi Hava sadzamvera. Chinthu chimene akanachita Adamu ndiko kupereka nsembe mwa kuotcha nyama. Imeneyi ndiyo inali njira yake yopempherera kwa Mulungu.